MUKANI PHUNZITSANI

Phunziro 1 - ZA MULUNGU WOSADZIWIKA

Mtumwi Paulo Anali Mthenga wa Mulungu. Paulo anali kumdziwa Mulungu woona. Mulungu anadzionetsa Yekha kwa Paulo kupyolera mu Mau Ace Oyera. Paulo anali kuyenda maulendo ambiri ku malo osiyana-siyana kukawadziwitsa anthu za Mulungu woona.

Pa ulendo wina Paulo anafika ku mzinda waukulu, dzina lace Atene. AkuAtene anali anthu anzeru kwambiri. Ndiponso anali anthu opembedza mafano. Iwo anali kukhulupilira milungu yambiri yosiyana-siyana. Anamanga maguwa a nsembe ndi macalici ambiri kwa milunguyo. Koma sanali kudziwa Mulungu woona ndani. Pa guwa la nsembe lina Paulo anapeza mau awa amene analembedwapo: KWA MULUNGU WOSADZIWIKA. Paulo anaima pa mbali pa guwalo nalalikira kwa anthuwo akuAtene. Iye analalikira kwa iwo za Mulunguyo amene iwo sanamdziwe Iye. Paulo anawauza kuti Mulungu Wosadziwikayo ndiye Mulungu woona yekha. Ndiye Mulungu amene analenga zinthu zonse napatsa moyo kwa anthu onse. Mulunguyo alikufuna kuti anthu onse akhale ndi Iye ku nthawi yosatha. Ndiye cifukwa cace anamtumiza Mpulumutsi ku dziko la pansi. Mpulumutsiyo anagonjetsa ucimo ndi imfa m'malo mwa anthu onse. Mpulumutsiyo adzabweranso kudzaweruza anthu a mitundu yonse. Mulungu alikufuna kuti anthu onse alape macimo ao, ndikumkhulupilira Mpulumutsi uyu, kuti iwo akhale ndi Iye ku nthawi yosatha kumwamba.

Ifenso tiri amithenga a Mulungu woona. Mulungu watipatsa ife Mau Ace Oyera, amene atiuza za Mpulumutsi, Yesu Kristu. Nthawi iri yonse imene ife timakumana pamodzi, tifuna kukubweretserani coonadi conena za mpulumutsi uyu, ndiye Mulungu woona (Macitidwe 17:16-34).

Anthu ambirimbiri amakhulupilira kuti kuli Mulungu, Iwo angathe kudziwa kuti kuli Mulungu pamene amaona ntchito za Mulungu mu cilengedwe Cace. Tikaiona nyumba, tingadziwe kuti munthu wina anaimanga. Pamene anthu amaona mapiri, mitengo ndi mitsinje ya m'dziko la pansi, angathe kudziwa kuti zinthu zonsezi sizinakhaleko mwa izo zokha, koma n'zoonadi kunayenera kukhala wina wamphamvu, ndiye Mulungu, amene anazilenga zonsezi (Ahebri 3:4). Makamaka zakumwamba zikutiuza kuti kuli Mulungu wa nzeru yaikulu ndi wa mphamvu zonse (Masalmo 19:1).

Ndiye cifukwa cace Baibulo lili kutsimikizira kuti kuli Mulungu. Anthu onse angathe kuzindikira kopanda citsimikiza kuti kuli Mulungu amene anazilenga zinthu zonse. Aucitsiru okha sacikhulupilira ici (Masalmo 14:1). Mdiponso munthu alindi mau mkati mwace, amene amuuza kuti kuli Mulungu. Timacha mau amenewa cikumbu mtima ca munthu.

Cikumbu mtima ici cimamuuza munthu kuti kuli kucimwa kucita zinthu zoipa, mwa citsanzo: kuba, kunama, kupha, ndi zinanso. Cikumbu mtima cathu cimacitira umboni ku lamulo la Mulungu lolembedwa mu mtima wa munthu. Cifukwa ca ucimo mauwa a cikumbu mtima sali angwiro, ai. Koma alimobe (Aroma 2:15), ngakhale mu Mtima wa munthu wocimwa.

Ngakhale nchito za Mulungu mu cilengedwe Cace ndiponso cikumbu mtima ca munthu zimacitira umboni kuti kuli Mulungu, zinthuzi sizingathe kutiuza Mulungu woona ndani. Tikhoza kuzindikira ici poona milungu yonama yambiri kapena mafano, amene anthu akunja amapembedza. Ena amapanga mafano a mitengo ndi miyala. Enanso amalemekeza dzuwa, mwezi, nyenyezi, kapena nyama zakuthengo (Masalmo 86:5). AkuAtene, amene Paulo anaceza nawo, sanali kutsimikizira Mulungu woona ndani, Ndiye cifukwa cace analimanga guwa la nsembe "KWA MULUNGU WOSADZIWIKA."

Motero kutiuza coonadi ca Iye yekha, Mulungu watipatsa Mau Ace mu Cipangano Coyera. Mulungu anali kuyankhula ndi anthu Ace kupyolera mwa Mose (Eksodo 25:1). Mulungu anaika mau Ace m'kamwa mwa aneneri Ace (Yeremiya 1: 9). Mau akuti "atero Mulungu" amapezeka kawiri kawiri m'Cipangano Cakale. Yesu Kristu anali kuyankhula Mau a Mulungu mwa ndunji kwa anthu (Yohane 17:17). Mulungu anawapatsa alembi a Cipangano Catsopano mphamvu yakuti amcitire umboni.

MATHEDWE: Inu muli kudziwa kuti kuli Mulungu. Mungathe kuzindikira ici poona nchito za Mulungu mu cilengedwe Cace. Cikumbu mtima canu cikuuzani zoona izi. Koma zinthuzi sitingathe kukuuzani zofunika zonse za Mulungu woona, amene anakupulumutsani ku macimo anu onse. Zimenezi Mulungu yekha akutiuza mu Mau Ace a m'Baibulo Ndithudi, tikufuna kuphunzira zinthu zina za Mulungu woona, amene anatikonda kwambiri motero kuti anatipatsa Mwana Wace wobadwa yekha, kuti atipulumutse ife ku ucimo wathu.

Phunziro 1 - ZA MULUNGU WOSADZIWIKA

DZIWANI NKHANI (Macitidwe 17:16-34)

Pezani yankho loyenera mu ciganizo ciri conse:

1. Paulo anafika ku mzinda wochedwa
   - ( ) Yerusalemu.
   - ( ) Atene.
   - ( ) Roma.

2. Paulo anapeza guwa la nsembe lolembedwa motere
   - ( ) KWA MULUNGU WOSADZIWIKA.
   - ( ) KWA MULUNGU M'MODZI MWA ATATU.

3. Anthu akuAtene anali kukhulupilira kuti
   - ( ) kulibe Mulungu.
   - ( ) kuli Mulungu M'modzi yekha.
   - ( ) kuli milungu yambiri.

GWIRITSANI NCHITO PHUNZIRO LATHU

Lembani cizindikiro (✓) pa ciganizo ciri conse cimene ciri coona.

( ) 1. Munthu sangathe kudziwa kuti kuli Mulungu.

( ) 2. Nyenyezi zakumwamba zikutiuza kuti kuli Mulungu.

( ) 3. Cikumbu mtima cimatiuza kuti kuli Mulungu.

( ) 4. Tingathe kumdziwa Mulungu woona popanda Baibulo.

( ) 5. Baibulo likutiuza ife Mulungu woona ndani.

PHUNZIRANI BAIBULO

Kodi ndime iti ya m'Baibulo ikutiuza kuti milungu yonse ya mitundu ya anthu ndiyo mafano?

Masalmo 14:1 Masalmo 19:1 Masalmo 96:5 Yohane 17:17

LOWEZANI MU MTIMA

Yohane 3:16 "Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupilira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha."

Phunziro 2 - ZA MAU A MULUNGU

Filipo anali m'modzi wa otumidwa oyamba aCikristu. Mulungu anamuuza Filipo kuti apite ku malo aku mbali ya kumwela kwa mzinda wa Yerusalemu. Filipo anapita kumeneko, ndipo anaona munthu wakuAitiopiya, amene anali kuwerenga bukhu. Bukhulo linali bukhu la Yesaya, mneneri wa m'Cipangano Cakale. Filipo anamfunsa munthuyo, "Kodi muzindikira cimene muwerenga?" WakuAitiopiya anamuyankha, "Ndingathe bwanji, popanda munthu wonditsogolera ine?" Pemenepo Filipo anayamba kulongosola mau a m'Cipangano Cakale kwa munthuyo. Filipo anamsonyeza m'mene Malembo Opatulikawo anakwaniritsidwa ndi nchito ya Yesu Kristu. WakuAitiopiya anawakhulupilira mau a Filipo onena za Kristu, nampempha kuti abatizidwe. Filipo anambatiza iye ndipo anapita kutali. WakuAitiopiya anali wokondwera kwambiri pamene Filipo anamfotokozera coonadi ca Mau a Mulungu (Maceitidwe 8:26-40).

Baibulo ndi Mau a Mulungu. Poyamba ici ndi coona conena za Cipangano Cakale. Mu phunziro lapita tinaphunzira kuti Mulungu anali kuyankhula kupyolera mwa Mose ndi Aneneri akale. Yesu Kristu anacitira umboni wakuti Cipangano Cakale ndi Mau a Mulungu. Alembi a Cipangano Catsopano, cimene cinalembedwa itatha nthawi ya Kristu, analembanso Mau a Mulungu. Mwa citsanzo, Mtumwi Paulo anali kunena kawiri-kawiri kuti mau ace ali Mau eni eni a Mulungu (1 Atesalonika 2:13).

Mwa izi tizindikira kuti Cipangano Cakale ndiponso Cipangano Catsopano, zonse ziwiri, ziri Mau a Mulungu, ngakhale zinalembedwa ndi anthu. Alembi ao anali anthu oyera mtima a Mulungu (1 Petro 1:21). M'Cipangano Cakale muli mabukhu 39 olekana. M'Cipangano Catsopano muli mabukhu 27. Cipangano Cakale cinalembedwa m'Cihebri, cimene cinali cinenero ca anthu a Mulungu akale. Cipangano Catsopano cinalembedwa m'Cigriki, cimene cinali cinerero conenedwa kupitirira dziko lonse la pansi pa nthawi ya Kristu. Kucokera ku zinenero ziwiri izi Baibulo lathu lamasuliridwa mu zinenero zina zambiri (kuposa zikwi).

Koma kungatheke bwanji kuti bukhu limene linalembedwa ndi anthu likhale Mau a Mulungu? Mulungu anawapatsa Mau Ace powauzira. "Kuuzira" kutanthauza "kupumiramo." Mulungu anapumira mwa alembi a Baibulo mau eni eni amene ayenera kuwalemba. Tikhulupilira kuti liu liri lonse la m'Baibulo liri loona, lopanda conama (Yohane 17:17). Mwina anthu akhoza kufunsa funsoli: "Kodi ndi cifukwa ciani mipingo imene ichedwa yaCikristu siimaphunzitsa cimodzimodzi?" Cifukwa cace ndi cakuti anthu a mipingo yambiri samakhulupilira kuti liu liri lonse la m'Baibulo ndi Mau a Mulungu. Anthu oterewa akhoza kulandira mbali zina za m'Baibulo. Koma iwo samalandira mbali zina zimene sangathe kuzimva bwino ndi kulongosolamo lingana ndi maganizo ao ao. Iwo akuti m'Baibulo muli Mau a Mulungu, koma iwo sakhulupilira kuti Baibulo ndi Mau a Mulungu.

Tsono, cifukwa cace ndi ciani Mulungu anatipatsa Baibulo? Nanga colinga cace ndi ciani? Kodi Baibulo langokhala bukhu lokondweretsa kuwerenga, monga ngati bukhu la mbiri kapena bukhu la nthano? Aitu, Baibulo ndilo bukhu limene likhoza kutipatsa nzeru kufikira cipulumutso. Mtumwi Paulo analemba ici mu kalata yace yaciwiri kwa Timoteo (2 Timoteo 3:15). Baibulo silipatsa ife nzeru ya zinthu za pansi pano, ai. Koma limatiuza m'mene tingathe kupulumutsidwa kupyolera mu cikhulupiliro ca mwa Yesu Kristu, motero kuti tidzakhale ndi moyo wosatha pamodzi ndi Mulungu kumwamba. N'cifukwa cace tiyenera kucita cimene Kristu afuna kuti ticite. Tiyenera "kusanthula m'Malembo," ndiko kunena tiphunzire Baibulo mwa khama kuti tipeze mkatimo uthenga wa Mulungu wa moyo wosatha (Yohane 5:39).

MATHEDWE: Mpingo wathu wa Lutheran uli kuima pakati pa Baibulo. Sumapeza ziphunzitso zace zocokera ku nzeru za anthu, ai. Koma Mpingo wa Lutheran umaphunzitsa zoonadi za Mau a Mulungu zokha ndiponso m'mene zoonadi izi zakhazikitsidwa mwa Mpulumutsi, Yesu Kristu. Mpingo wa Lutheran ukufuna kuti inunso mudziwe cilingaliro ca Mulungu cakuti anthu onse apulumuke ku umoyo wosatha.

Phunziro 2 - ZA MAU A MULUNGU

DZIWANI NKHANI (Macitidwe 8:26-40)

Pezani yankho loyenera mu ciganizo ciri conse:

1. Filipo anakumana ndi munthu wa ku
   ( ) Ulaya.
   ( ) Amerika.
   ( ) Aitiopiya.

2. Munthuyo anali kuwerenga
   ( ) Gipangano Catsopano.
   ( ) Bukhu la Yesaya.
   ( ) Mabukhu a Mose.

3. Pamene Filipo analongosola Malembo Opatulika, munthu wakuAitiopiya.
   ( ) anakwiya ndi Filipo.
   ( ) anacoka mwa cisoni.
   ( ) anakhulupilira nabatizidwa.

GWIRITSANI NCHITO PHUNZIRO LATHU

Lembani cizindikiro (✓) pa ciganizo ciri conse cimene ciri coona.

( ) 1. M'Baibulo muli Mau a Mulungu.

( ) 2. Baibulo ndi Mau a Mulungu.

( ) 3. M'Baibulo muli zolakwa zina.

( ) 4. Liu liri lonse la m'Baibulo liri loona.

( ) 5. Tiyenera kuphunzira Baibulo lathu ndi khama.

( ) 6. Sitiyenera kuwerenga Baibulo cifukwa liri lobvuta kumva bwino.

PHUNZIRANI BAIBULO

Kodi ndime iti ya m'phunziro lathu lalero ikutiuza kuti Mzimu Woyera anawauza alembi oyera mtima mau amene ayenera kulemba?

2 Petro 1:21 Yohane 17:17 2 Timoteo 3:15

LOWEZANI MU MTIMA

Mabukhu a m'Cipangano Cakale (39)

Genesis	Mafumu (2)	Nyimbo ya Solomo	Obadiya
Eksodo	Mbiri (2)		Yona
Levitiko	Ezara	Yesaya	Mika
Numeri	Nehemiya	Yeremiya	Nahumu
Deuteronomo	Estere	Maliro	Habakuku
		Ezekieli	Zefaniya
Yoswa	Yobu	Danieli	Hagai
Oweruza	Masalmo	Hoseya	Zekariya
Rute	Miyambo	Yoweli	Malaki
Samueli (2)	Mlaliki	Amosi	

Phunziro 3 - ZA MULUNGU WOONA YEKHA

Zaka zambiri zapitazo kunali mfuma ya mphamvu yaikulu. Mfumuyo inali kulamulira anthu ambiri, maiko ambiri, ndiponso ng'ombe zambiri. Koma mfumu imeneyo inali kubvutika mu mtima mwace. Iyo inali kufuna kudziwa zinthu zina zambiri za Mulungu. Mfumuyo inadziwana ndi munthu wina wa nzeru yopambana kwambiri. Tsiku lina mfumuyo inamfunsa wanzeruyo, "Kodi Mulungu ndani?" Wanzeruyo anaganizira pa ici nthawi yaitali. Pomariza iye anati kwa mfumu, "Ndipatseni tsiku limodzi lakuti ndiganizirepo pamenepa, ndipo ndidzakuyankhani." Tsiku lamawa linafika, koma wanzeruyo sanalipeze yankho loyenera. Nthawi imemeyi anati kwa mfumuyo, "Ndipatseni masiku awiri ena, ndipo ndidzakuuzani za Mulungu." Patapita masiku awiri wanzeruyo sanapezebe yankho. Ndipo iye anaipempha mfumuyo kuti impatse masiku anai ena kuti aganizire funsolo. Izi zinali kupitirira nthawi yaitali. Nthawi ili yonse wanzeruyo anaipempha mfumu kuti impatse nthawi yinanso yakuganizira funsolo. Koma sanalipeze yankho konse. Pomaliza mfumuyo inayanba kukalipa. Iyo inaumirira, "Cifukwa ndi ciani sunandipatseko yankho?" Wanzeruyo anati, "Ngakhale ndiri kuganizira pa funsoli mwa cangu, kunena zoona ine sindingathe kupeza yankho loyenera, ai. Mulungu ndani? Mulungu ndi ciani? Kayatu, ine sindidziwa."

Anzeru onse a m'dziko lapansi alepheradi kuyankha funsoli. Yankho lokha loyenera likupezeka m'Baibulo. Tiyeni timve yankho limene Mulungu akutipatsa za Iye yekha mu Mau Ace Oyera.

Paciambi, Baibulo likutiuza kuti Mulungu ndiye mzimu (Yohane 4:24). Mzimu ndi munthu wopanda mnofu ndi mafupa (Luka 24:39). Simukhoza kuuona mzimu. Ganizirani pa magetsi. Mungathe kuona kuwala kumene kumacitidwa ndi magetsi. Koma simukhoza kuona mphamvu yace yodabwitsa pamene iri kuyendera mwayala. Komabe Mulungu ali wopambana mphamvu yonga magetsi imene simungathe kuiona. Mulungu ali wapadera. Iye anati kwa Mose, "INE NDINE YEMWE NDIRI INE."

Baibulo likutiuzanso zinthu zambiri za Mulungu. Likutiuza kuti Mulungu ali wacikhalire (Masalmo 90:2). Iye ali wosayambira ndiponso wosatha. Kodi mungathe kumva ici ndi nzeru zanu? Mulungu ali wosasinthika (Malaki 3:6). Nthawi zonse Iye ali cimodzimodzi, kapena pa nthawi yathu ya cimwemwe, kapena pa nthawi yathu ya cisoni. Mulungu ali wamphamvu zonse (Genesis 17:1). Palibe kanthu komulephera Iye. Ndithu, Iye angathe kucita cinthu ciri conse cimene Iye afuna. Mulungu ali wanzeru zonse (Yohane 21:17). Iye ali kudziwadi zinthu zonse za ife, angakhale maganizo athu acinsinsi. Mulungu ali paliponse (Yeremiya 23:24). Iye adzala kumwamba ndi dziko la pansi. Sitingathe kubisala ife tokha kwa Mulungu. Mulungu ali woyera (Levitiko 19:2). Palibe kanthu kalikonse kocimwa kamene kangathe kuima pa maso pace. Poyamba ucimo wathu uyenera kucotsedwa. Mulungu ali wokhulupirika (2 Timoteo 2:13). Iye amasunga malonjezo a m'Mau Ace. Tikhoza kumkhulupilira Iye. Mulungu ali wacifundo (Masalmo 145:9). Ici citanthauza kuti awacitira cokoma iwo amene ali wosayenera ubwino Wace. Mulungu ndiye cikondi (1 Yohane 4:8). Cifukwa ca cikondi Cace Mulungu anapereka Mwana Wace Yekha kuti atifere ife pa mtanda.

Mulungu uyu wadzionetsa yekha kwa ife mu Baibulo monga Mulungu M'Modzi mwa Atatu. Mulungu wadzionetsa yekha mwa Anthu atatu: Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera (Mateyu 28:19). Anthu atatu awa ali m'modzi ndi mphamvu ndiponso ulemelero. Atate ndiye Mulungu. Mwana, Yesu, Kristu, ndiye Mulungu. Mzimu Woyera ndiye Mulungu. Koma kulibe milungu itatu, koma Mulungu m'modzi yekha (Deuteronomo 6:4).

Baibulo likutiuza kuti nthawi yina Anthu atatu onsewo anadzionetsa okha pa nthawi imodzi. Ici cinacitika pa nthawi ya kubatizidwa kwa Kristu (Mateyu 3:13-17). Pamenepo Atate anayankhula mau kucokera kumwamba. Mwana, Yesu Kristu, anabatizidwa ndi Yohane Mbatizi. Mzimu Woyera anaoneka mu maonekedwe a nkhunda imene inatisika kucokera kumwamba.

MATHEDWE: Ife sitingathe kumva bwino kumene kungakhale Anthu atatu, amene ali m'modzi mu mphamvu ndi ulemelero, koma Mulungu m'modzi yekha. N'zoonadi Mulungu ali wopambana nzeru zathu. Munjira iyi Mulungu wadzionetsa yekha kwa ife m'Baibulo: Atate anamtumiza Mwana Wace kuti akhale Mpulumutsi wathu; Mwana anatiombola ife ndi kusauka Kwace ndi imfa Yace pa mtanda; Mzimu Woyera amabweretsa zinthu zonse zimene Kristu waticitira ife. Khulupilirani Uthenga Wabwino uwu wa Mulungu ndi mtima wanu wonse ndipo mudzapulumutsidwa!

Phunziro 3 - ZA MULUNGU WOONA YEKHA

WERENGANI MATEYU 3:13-17

Pa nthawi ya ubatizo wa Yesu Kristu, Munthu aliyense wa Mulungu M'modzi mwa Atatu anadzionetsa yekha mu njira yapadera. Pezani njirayo yoyenera Munthu aliyense amene walembedwa pansipa:

Mulungu Atate	_____	a. Amene Yohane anambatiza Iye.
Mulungu Mwana	_____	b. Nkhunda.
Mulungu Mzimu Woyera	_____	c. Mau ocokera kumwamba.

GWIRITSANI NCHITO PHUNZIRO LATHU

Lembani cizindikiro (✓) pa ciganizo ciri conse cimene ciri coona.

( ) 1. Mulungu woona yekha wadzionetsa mwa Anthu atatu.

( ) 2. Anthu atatuwo ali milungu itatu.

( ) 3. Anthu atatuwo ali m'modzi mu mphamvu.

( ) 4. Atateyo ali wopambana Mwana ndi Mzimu Woyera.

( ) 5. Timamucha Mulungu woonayu, dzina Lace Mulungu M'modzi mwa Atatu.

PHUNZIRANI BAIBULO

Ndime zotsatirazi za m'Baibulo zikutiuza zina za Mulungu:

Masalmo 90:2	Malaki 3:6	Genesis 17:1	Yohane 21:17	Yeremiya 23:24	Livitiko 19:2
2 Timoteo 2:13		Masalmo 145:9		1 Yohane 4:8	

Kodi ndime ziti zikutiuza ife kuti:

Mulungu amadziwa maganizo athu? _____

Mulungu ali paliponse? _____

LOWEZANI MU MTIMA

Mabukhu a m'Cipangano Catsopano (27)

Mateyu	Aroma	Atesalonika (2)	Petro (2)
Marko	Akorinto (2)	Timoteo (2)	Yohane (3)
Luka	Agalatiya	Tito	Yuda
Yohane	Aefeso	Pilemoni	
	Afilipi	Ahebri	Cibvumbulutso
Macitidwe	Akolose	Yakobo	

Phunziro 4 - ZA CILENGEDWE

(Genesis, mitu 1 ndi 2) Paciyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Mulungu asanapange zinthu zonse, kunalibe kanthu kali konse—kunalibe mitengo, miyala, mphepo, kapena anthu. Pa tsiku loyamba Mulungu anati, "Kuyere;" ndipo kunayera. Pa tsiku laciwiri Mulungu analenga thambo mu njira yomweyo. Pa tsiku lacitatu Mulungu analekanitsa nthaka ndi madzi nakulitsa maudzu, mitengo, ndi zomera zina pa nthakayo. Pa tsiku lacinai Mulungu analenga dzuwa, mwezi, ndi nyenyezi zonse. Pa tsiku lacisanu Mulungu anazipanga nsomba ndi nyama zina zimene ziri kukhala m'madzi, ndiponso mbalame za mlengalenga. Pa tsiku lacisanu ndi cimodzi Mulungu anapanga nyama za pa mtunda, ndiponso munthu. Zonse zimene Mulungu anazilenga zinali zabwino ndithu. Pa tsiku lacisanu ndi ciwiri Mulungu anapumula ndipo analiyeretsa tsikulo.

Mulungu analenga zonse zakumwamba ndi za dziko lapansi ndi mphamvu ya Mau Ace. Mulungu ananena ndipo kunacitika. Koma panali kusiyana kumodzi. Pamene Mulugu anampanga munthu pa tsiku lacisanu ndi cimodzi, Iye anamuumba ndi dothe lapansi. Pamenepo Mulungu anauzira mpweya wa moyo m'mphuno mwace ndipo munthuyo anakhala wa moyo. Mulungu anamlenga munthu mu cifanizo Cace. Ici citanthauza kuti munthu anali woyera ndiponso wopanda ucimo pamene Mulungu anamlenga iye. Munjira iyi Mulungu analenga Adamu, munthu woyamba. Pamene Mulungu anaona kuti Adamu anali wopanda mnzace, Iye anamgonetsa Adamu tulo tatikulu. Ndipo anatengako nthiti ya Adamu imodzi namupanga mkazi woyamba kucokera ku nthitiyo. Mulungu anabwera naye kwa Adamu, ndipo Adamu anamucha Hava. Mulungu anawaika Adamu ndi mkazi wace, Hava, mu munda wokongola kwambiri wochedwa Paradiso. Mulungu anawadalitsa nawauza kuti alidzaze dziko lapansi ndi ana ao ndi kulamulira zinthu zonse zimene Iye anawapangira iwo.

Pakati pa mundawo Mulungu anadzalapo mitengo iwiri. Wina unachedwa Mtengo wa Moyo ndi winanso unachedwa Mtengo Wakudziwitsa Zabwino ndi Zoipa. Mulungu anawapatsa Adamu ndi Hava lamulo lakuti asadye cipatso ca Mtengo Wakudziwitsa Zabwino ndi Zoipa. Anawauza kuti tsiku lomwe adzadya umenewo adzafa ndithu. Mulungu anacita ici kuti awayese Adamu ndi Hava. Iye anafuna kudziwa ngati iwo adzamvera lamulo Lace.

Mu njira iyi yacidule Baibulo likutiuza m'mene zinthu zonse zinapangiridwa. Mulungu anazilenga zinthu zonse zakumwamba ndi za pansi pano mu masiku asanu ndi limodzi (Eksodo 20:11). Angelo analengedwanso ndi Mulungu nthawi imeneyo, koma Baibulo silikutiuza ife tsiku limene analengedwa. Tikhoza kuzindikira kuti mbiri ya cilengedwe imene iri kupezeka m'Baibulo iri yosiyana kwambiri ndi zinthu zimene zimaphunzitsidwa ndi anzeru ambiri a m'dziko lapansi masiku ano. Makamaka iwo amaphunzitsa kuti dziko lapansi linali kukula kupitirira nthawi ya saka zoposa zikwizikwi. Ciphunzitso ici cimachedwa 'evolution.' Aphunzitsi ace ali kufuna kupeza yankho la nzeru limene likhoza kufotokoza za gwero la zinthu zonse. Koma aphunzitsi oterewo ali opanda nzeru mu ziphunzitso zao. Amanena zinthu zambiri zimene sizinatsimikizidwe ndi zoona zeni zeni. Iwo sangathe kulongosola m'mene zinthu zonse zinayambira.

Baibulo likusonyeza kuti munthu ali wopambana zolengedwa zina zonse cifukwa Mulungu anamlenga munthu mu cifanizo Cace (Genesis 1:27). Ici sicitanthauza kuti munthu akuoneka monga Mulungu ai. Koma cifanizo ca Mulungu ndi cilungamo ndi ciyero cangwiro. Mtumwi Paulo akutiphunzitsa ici ponena kuti munthu analengedwa monga mwa Mulungu, m'cilungamo ndi m'ciyero ca coonadi (Aefeso 4:24).

Koma Mulungu sanazilenge zinthu zonse kuti zikhalebe ndi mphamvu zao zao ai. Ndithu Mulungu ali kuzisunga ndi kuzisamalira zinthu zonse. Iye amanyamula zinthu zonse ndi Mau Ace a mphamvu yonse (Ahebri 1:3). Dziko lapansi silingathe kupitirira kamphindi kakang'ono kopanda thandizo la Mulungu. Tsiku ndi tsiku Mulungu amatipatsa zofunika zonse kuti tisamalire thupi ndi moyo wathu. Cifukwa ca zonsezi tiyenera kumyamika Mulungu ndi kumvera Mau Ace nthawi zonse (Masalmo 118:1).

MATHEDWE:
Timyamikire Atate,
Ndi Mwana Wace 'kondedwa;
Titama Mzimu Woyera:
Mulungu wodalitsidwa. Amen.

Phunziro 4 - ZA CILENGEDWE

DZIWANI NKHANI (Genesis 1)

Zinthu zimene Mulungu anazipanga mu masiku asanu ndi limodzi a cilengedwe Cace zalembedwa pansipa. Lembani mzera wolumikizana ndi zinthuzi ndi tsiku lace limene Mulungu anazilenga.

Nyanja, Mitsinje	Tsiku loyamba
Dzuwa, Mwezi, Nyenyezi	Tsiku laciwiri
Nsomba, Mbalame	Tsiku lacitatu
Munthu, Nyama	Tsiku lacinai
Kuyera	Tsiku lacisanu
Thambo	Tsiku lacisanu ndi cimodzi

GWIRITSANI NCHITO PHUNZIRO LATHU

Lembani cizindikiro (✓) pa yankho liri lonse limene liri loona:

1. Mulungu anamlenga munthu mu cifanizo Cace. Ici cikutanthauza kuti

   ( ) munthu anapangidwa kuti aoneke monga Mulungu.
   ( ) munthu analengedwa woyera ndi wopanda ucimo.

2. Mulungu anampatsa munthu lamulo lakuti asadye cipatso ca Mtengo Wakudziwitsa Zabwino ndi Zooipa.

   ( ) cifukwa Iye anafuna kuyesa kumvera kwace kwa munthu.
   ( ) cifukwa Iye anafuna munthu kuti akhale osaphunzira.

3. Mulungu ali kutipatsa cakudya ndi zobvala nthawi ndi nthawi

   ( ) cifukwa timazigwirira nchito molimbika.
   ( ) cifukwa ife tiri anthu abwino.
   ( ) cifukwa Mulungu ali wa cikondi ndi wa cisomo.

4. Mulungu akufuna kuti timyamike Iye cifukwa ca madalitso Ace onse.

   ( ) pa tsiku la Mulungu lokha.
   ( ) pa tsiku liri lonse la moyo wathu.

PHUNZIRANI BAIBULO

Kodi ndime iti ya m'Baibulo ikutiuza kuti Mulungu ali kusungabe zinthu zonse.

Genesis 2:17 Ahebri 1:3 Genesis 1:27 Eksodo 20:11

LOWEZANI MU MTIMA

NDIME YOYAMBA YA MAU A CIBVOMEREZO CA ATUMWI

Ndikhulupilira Mulungu Atate wa mphamvu zonse, Wolenga za kumwamba ndi za pansi.

Kodi ici citanthauzanji?

Ndikhulupilira kuti Mulungu anandipanga ine ndi zonse za moyo, pondipatsa ine thupi ndi moyo, maso, makutu, ndi ziwalo zanga zonse, nzeru, ndi maluso anga onse.

Phunziro 5 - ZA KUGWA KWA MUNTHU MU UCIMO

(Genesis 3) Zinthu zonse zimene zinalengedwa ndi Mulungu zinali zabwino ndithu. Adamu ndi Hava anali opanda ucimo. Iwo anali kukhala m'munda wokongola kwambiri, dzina lace Edene. Koma tsiku lina mdierekezi, mu maonekedwe a njoka, anayankhula ndi Hava namuuza kuti asamvere lamulo la Mulungu. Hava anamvera mau a njokayo nayamba kukaika kaika ndi mau a Mulungu. Zipatso zoletsedwa za Mtengo Wakudziwitsa Zabwino ndi Zoipa zinaoneka zabwino kwa iye. Hava anadya zipatso zina za mtengowo ndipo anampatsa mwamuna wace Adamu kuti adyenso. Mu njira imeneyi ucimo unalowa mu mitima yao. Onse awiriwo anagwidwa ndi mantha ndipo anayesa kubisala kwa Mulungu. Pamene Mulungu anawapeza iwo, Adamu anayesa kumtulira mlandu Hava, ndipo Hava anayesa kuitulira mlandu njokayo. Ici cikusonyeza kuti iwo anataya cifanizo ca Mulungu. Iwo anayenera kulangidwa ndi imfa ndi cionongeko cosatha. Mulungu anawauza kuti acoke m'mundamo. Iye anawauzanso kuti ayenera kugwira nchito ya thukuta kuti apeze cakudya ca tsiku ndi tsiku. Minga ndi zirombo zina zidzacuruka mu minda yao. Koma Mulungu anawapatsa lonjezo lodabwitsa. Hava adzabala ana. Kucokera mwa anawo Mpulumutsi wa dziko lapansi adzadza. Mpulumutsiyo adzalalira mutu wa njokayo. Ici cikutanthauza kuti Iye adzaononga mphamvu yace ya mdierekezi pamwamba pa anthu.

Nkhaniyi yonena za kugwa kwa munthu mu ucimo ikhoza kuputa mafunso ambiri. Kodi coipa cinacokera kuti? Kodi ndani anali kuyankhula m'kamwa mwa njokayo? Kodi cifukwa n'ciani Mulungu analola kuti coopsya cimeneco cicitike? Baibulo silikuyankha mafunso onsewa kwa ife. Palibe lamulo lakuti Mulungu alungamitse njira Zace pocita nao anthu. Koma Mulungu akhale Mulungu ndipo timuyamike Iye cifukwa anatiuza zonse zofunika zimene tiyenera kudziwa kuti tipulumutsidwe.

Baibulo limatiuza kuti zonse zimene zinapangidwa ndi Mulungu mu masiku asanu ndi limodzi a cilengedwa Cace zinali zabwino ndithu (Genesis 1:31). Paciyambi angelo onse amene analengedwa ndi Mulungu anali angwiro. Koma Baibulo limatiuzanso kuti patapita nthawi angelo ena ambiri anamcimwira Mulungu ndipo Iye anawacotsakumwamba (2 Petro 2:4). Baibulo limatiuza kuti mdierekezi amene ali mtsogoleri wa angelo onse oipawo, amagwiritsa nchito mphamvu yace yaikulu kuti anyenge anthu a m'dziko lapansi. Iye, amene achedwanso Satana, ali kufuna kuti anthu onse atayike asamumvere Mulungu. Mdierekezi ndiye njokayo amene anamyesa Hava mu Munda wa Edene (Cibvumbulutso 12:9). Anabwera kwa Hava ndi zonama ndi zonyenga zace zonse namcimwitsa iye pakudya cipatso coletsedwa.

Zotsatira zoopsya za kugwa mu ucimo zalandiridwa ndi anthu onse. Mwana wace woyamba wa Adamu sanabadwe mu cifanizo coyera ca Mulungu, koma mu cifanizo ca ucimo wa munthu (Genesis 5:3). Baibulo limatiuza momveka bwino kuti anthu onse amabadwa mu ucimo (Masalmo 51:5). Yesu anati kwa Nikodemo, "Cobadwa m'thupi cikhala thupi." Ndi liu lakuti "thupi," Yesu anatanthauza mabadwidwe a ucimo wa anthu onse. Anamuuza Nikodemo kuti cifukwa ca mabadwidwe a ucimo, anthu ayenera "kubadwa mwatsopano" ndi madzi ndi Mzimu Woyera kuti apulumutsidwe kucokera ku mphamvu ya mdierekezi ndi ucimo. Ife tikhoza kuphunzitsidwa za ucimo cifukwa zoipa zakhala kale m'kati mwao kuyambira nthawi ya kubadwa kwao. Cimoli limene anthu onse amabadwamo limachedwa <u>ucimo wacibadwidwe</u>.

Cifukwa ca ucimo munthu aliyense ayenera kulangidwa. Mtumwi Paulo akutiuza kuti "mphotho yace ya ucimo ndi imfa" (Aroma 6:23). Pogwiritsa nchito liu lakuti "imfa," ali kutanthauza imfa yosatha kapena cionongeko ku Hade. Ife sitikhoza kumtulira mlandu Mulungu cifukwa ca ici, ai. Koma makamaka timyamike Mulungu cifukwa, Adamu ndi Hava atagwa mu ucimo, nthawi imeneyo Iye anawapatsa lonjezo la Mpulumutsi amene adzacotsa ucimo wao (Genesis 3:15). <u>Lonjezo loyambalo la Uthenga Wabwino</u> linawauza za mbeu ya mkazi (Mpulumutsi), imene idzalalira mutu wa njokayo (mphamvu ya mdierekezi).

MATHEDWE: Inu ndinu munthu wocimwa. Munabadwa mu ucimo. Tsiku ndi tsiku mumacimwira Mulungu mu maganizo, mau, ndi nchito zanu. N'zoonadi muyenera kulangidwa ku nthawi yosatha. Koma tamvetsetsani Uthenga Wabwino: Mulungu anakutumizirani Mpulumutsi, Yesu Kristu, amene analipira macimo anu onse ndi imfa Yace pa mtanda. Khulupilirani mwa Iye ndipo mudzapulumutsidwa!

Phunziro 5 - ZA KUGWA KWA MUNTHU MU UCIMO

DZIWANI NKHANI **(Genesis 5)**

Lembani cizindikiro (✓) pa ciganizo ciri conse cimene ciri coona.

( ) 1. Angelo onse anali opanda ucimo pamene Mulungu anawalenga.

( ) 2. Satana anali mngelo wina amene anapandukira Mulungu.

( ) 3. Njokayo inayankhula ndi Hava ndi mphamvu yace yokha.

( ) 4. Pocimwa pace Hava anali ndi mlandu waukulu kuposa Adamu.

( ) 5. Adamu ndi Hava anabisala kwa Mulungu cifukwa anali amarisece.

( ) 6. Adamu ndi Hava anayenera kulangidwa ndi imfa yosatha.

( ) 7. Mulungu anaonetsa cikondi Cace cacikulu pakulonjeza za Mpulumutsi.

GWIRITSANI NCHITO PHUNZIRO LATHU

Pamene iwo anacimwa, Adamu ndi Hava anataya cifanizo ca Mulungu. Kodi cifukwa ca ici, ciani cinacitika kwa anthu onse? Lembani cizindikiro (✓) pa ciganizo ciri conse cimene ciri coona:

( ) 1. Ana a Adamu ndi Hava anabadwa mu cifanizo ca Mulungu.

( ) 2. Anthu onse amabadwa mu ucimo.

( ) 3. Tiana tingathe kucimwa pakungoona makhalidwe cipa a anthu ena okha.

( ) 4. Tikayesetsa kwambiri, tingakhale ndi moyo wa ngwiro.

( ) 5. Ciyembekezo cathu cokha ca cipulumutso cikupezeka mwa Kristu.

PHUNZIRANI BAIBULO

Lembani mzera pansi pa ndime ya m'Baibulo imene ikutiuza za lonjezo loyamba la Mulungu lonena za Mpulumutsi:

Aroma 6:23 Cibvumbulutso 12:9 Genesis 3:15 Genesis 1:31

PHUNZIRANI KATIKISIMU

NDIME YOYAMBA YA MAU CIBVOMEREZO CA ATUMWI

Ndikhulupilira mwa Mulungu Atate wa mphamvu zonse, wolenga za kumwamba ndi za pansi.

Kodi ici citanthauzanji?

(Mau ali kupitirira)

Iye amandisungabe ine pondipatsa zocuruka tsiku ndi tsiku: zobvala ndi nsapato, cakudya ndi kumwa, nyumba ndi banja, mkazi ndi ana, dziko, zoweta, ndi cuma canga conse, ndi zonse zofunika zoti ndisunge thupi ndi moyo wanga. Iye akundicinjiriza ine pa zoopaya zonse ndi kunditeteza pa coipa ciri conse. Ndipo Iye amandicitira zonsezi cifukwa ca ubwino Wace ndi cifundo Cace basi, ngakhale ndiri wosayenera. Cifukwa ca zonsezi ine ndiyenera kumyamika ndi kumlemekeza Mulungu, ndi kumtumikira ndi kumumvera Iye. Ndithu, izi ndi zoonadi.

Phunziro 6 - LAMULO NDI UTHENGA WABWINO

(Eksodo, mitu 19 ndi 20) Adamu ndi Hava atamwalira, anthu a m'dziko lapansi anayamba kucuruka, koma iwo anayambanso kukhala anthu oipa kwambiri. Ndi cifukwa cace Mulungu anawalanga potumiza cigumula cacikulu. Noah ndi banja lace lokha anapulumutsidwa mu combo. Komabe ucimo unali kupitirira ndi kukula. Pamene anthu anayesa kumanga nsanja yaitali ya ku Babele yoti ikafike kumwamba, Mulungu anawasokonezetsa ciyankhulo cao, ndipo anthuwo anayamba kubalalika kupitirira dziko lapansi. Koma Mulungu anali wokhulupirika ku konjezo Lace loti adzataumiza Mpulumutsi. Iye anapatsanso lonjezo ili kwa Abrahamu, Isake, ndi Yakobo, ndipo anawapatsa dziko lotchedwa Kanani kuti likhale dziko lao la lonjezo. Yakobo ndi banja lace lonse anayenda ulendo waukulu wopita ku dziko la Igupto cifukwa ca njala yoopsya kwao ku Kanani. Pokhala mu Igupto, anthuwo anacuruka kwambiri nakhala mtundu waukulu. Koma patapita nthawi Aigupto anayamba kuwazunza kwambiri ndipo Aisrayeli anali kugwira nchito ya thukuta monga akapolo. Pamenepo Mulungu anamuitana Mose kuti awatsogolere anthu ace kucokera mu Igupto kubweranso ku dziko lolonjezedwa la Kanani.

Pamene anthu a Mulungu anali kuyenda kunka ku Kanani, Mulungu anaonekera kwa iwo pa Phiri la Sinai ndi mabingu, zimphezi, ndi mtambo wakuda bii. Mose anakwera pa phirilo nakhalapo masiku makumi anai. Pamenepo Mulungu anapereka Cilamulo Cace kwa Mose. Anaperekanso malamulo ena ambiri olamulira anthuwo ndi malamulo akumpembedza mu Kacisi. Koma pamwamba pa zonsezi Mulungu analemba Malamulo Khumi pa magome a miyala awiri. Malamulo Khumiwo anali Cilamulo cangwiro ca Mulungu. Anthu onse ayenera kumvera Malamulo awa nthawi zonse. Mwa iwo Mulungu akuwauza anthu zoyenera zoti iwo acite ndi zoti asacite kuti akhale ndi moyo womkondweretsa Iye.

Paciyambi pamene Mulungu anamlenga munthu, Iye analemba malamulo Ace mu mtima wa munthu. Adamu anakhoza kumva cifuniro Cace ca Mulungu mwangwiro. Koma pakugwa mu ucimo munthu anataya nzeru zace zangwiro za malamulo a Mulungu. Cifukwa ca ici tsopano anthu onse ali adani a Mulungu mwa cibadwidwe. Maganizo ao ali osokonezeka. Zinthu za Mulungu ziri sopusa kwa anthu (Aroma 5:12, 1 Akorinto 2:14). Cingakhale cinthuci ciri coona, munthu angathe kuzindikira kusiyana kwace kwa zabwino ndi zoipa. Cikumbu mtima cace, cingakhale siciri cangwiro, ciri kucitira umboni za malamulowo amene analembedwa mu mtima wa munthu. Angakhale anthu akunja amaonetsa nchito ya malamulowo olembedwa m'mitima yao (Aroma 2:15).

Cifukwa mwa cibadwidwe nzeru ya munthu yonena za malamulo a Mulungu siri ya ngwiro, Mulungu anapereka malamulo Ace kupyolera mwa Mose (Deuteronomo 10:4). Malamulo Khumiwo amatiuza cifunira coyera ca Mulungu. Iwo amatilamulira kuti timvere Mulungu mwangwiro (Levitiko 19:2). Ife sitiloledwa kulakwa konse molingana ndi mau a Malamulo Khumi.

Kunena zoona, palibe munthu aliyense angathe kusunga malamulo a Mulungu mwangwiro (Aroma 3:23). Tikhoza kuzindikira ici pophunzira Malamulo Khumi limodzi-limodzi. Pamene tidzifanizira tokha ndi Lamulo la ngwiro la Mulungu tingathe kudziwa kuti ife tiri anthu ocimwadi (Aroma 3:20). Tikhoza kumva cifukwa ciani tingathe kutembereredwa ndi Mulungu cifukwa ca macimo athu (Deuteronomo 27:26). Tikhoza kufanizira Lamulo la Mulungu ndi glas (kalilole). Kawiri kawiri anthu amapenyetsetsa pa 'glas' kuti aone ngati nkhope zao zili zoyera ndiponso ngati tsitsi lao liri lopeseka bwino. N'cimodzi-modzi ife Akristu timapenyetsetsa pa 'glas' la Lamulo la Mulungu. Pa 'glas' lopatulika ili tingaonemo macimo athu ambiri amene amatitsutsa ife pa maso pa Mulungu.

Anthu ali naco ciyembekezo cimodzi cokha coti angaime pa maso pa Mulungu. Ici ndi lonjezo la Mulungu lonena za cipulumutso ca mwa Yesu Kristu. Zimene malamulo sangathe kucita, Mulungu amazipereka kwa ife mwa Kristu (Yohane 1:17). Tiwacha Mau Abwino awa acipulumutso cathu ca mwa Yesu Kristu Uthenga Wabwino. Liu liri lonse la m'Baibulo limene likulonjeza cikhululukiro ndi ciyembekezo coona kwa anthu ocimwa ndi ciphunzitso ceni ceni ca Uthenga Wabwino.

MATHEDWE: Ziphunzitso Ziwiri zofunika za m'Baibulo ndi MALAMULO ndi UTHENGA WABWINO. MALAMULO anatiuza zifuniro Zace za Mulungu ndi kutidziwitsa ucimo ndi ciweruzo cathu. UTHENGA WABWINO umatiuza cikondi Cace ca Mulungu ndi kutidziwitsa cipulumutso cathu ca mwa Yesu Kristu. Ife timafunitsitsa ziphunzitso ziwirizi. Malamulo a Mulungu ayenera kutsutsa ucimo wathu ndi kutisonyeza kusowa kwathu kwa Mpulumutsi. Pamenepo mau a Uthenga Wabwino wa Kristu ukhoza kulandiridwa ndi ife ndipo tidzafunadi kumtumikira Mulungu ndi miyoyo yathu yonse.

Phunziro 6 - LAMULO NDI UTHENGA WABWINO

DZIWANI NKHANI

Maina otsatirawa akupezeka mu phunziro lathu la lero. Kodi ndani anayamba kubadwa? Lembani nambala 1 pa dzina lace. Lembani nambala 2 pa dzina la munthuyo amene anali waciwiri kubadwa. Citani cimondzi-modzi ku maina onse.

( ) Mose
( ) Isake
( ) Adamu
( ) Abrahamu
( ) Yakobo
( ) Noah

GWIRITSANI NCHITO PHUNZIRO LATHU

Ziphunzitso ziwiri zofunikadi za m'Baibulo ndi MALAMULO ndi UTHENGA WABWINO. Lembani (M) pa ciganizo ciri conse cimene ciri kunena za MALAMULO. Lembani (U) pa ciganizo cimene cikutiuza za UTHENGA WABWINO.

( ) 1. Cikutiphunzitsa zinthu zoti ticite ndiponso zoti tisacite.

( ) 2. Cikutiphunzitsa zinthu zimene Mulungu anaticitira ife ndiponso zimene ali kuticitirabe ife.

( ) 3. Cikutiuza za cikondi ca Mulungu mwa Kristu.

( ) 4. Cikutiuza za cilango ca Mulungu kwa onse ocimwa.

( ) 5. Cikutidziwitsa Mpulumutsi wathu.

( ) 6. Cikutidziwitsa ucimo wathu.

PHUNZIRANI BAIBULO

Lembani mzera pansi pa ndime za m'phunziro lathu zimene ziri ndi lonjezo la Uthenga Wabwino.

Yohane 1:17 Aroma 3:25 Deuteronomo 27:26 Aroma 1:16

LOWEZANI MU MTIMA

Aroma 3:28 Pakuti tikuyesa munthu wolungama cifukwa ca cikhulupiliro, wopanda nchito za lamulo.

Phunziro 7 - ZA LAMULO LOYAMBA

(Danieli, Mutu 3) Anthu a Mulungu anali kukhala m'dziko la cilendo, dzina lace Babulo. Mulungu analola Nebukadinezara, mfuma wa ku Babulo, kuti awagwire anthuwo cifukwa iwo anasiya Mau a Mulungu. Anthu a ku Babulo sanali kumkhulupilira Mulungu woona. Iwo anali kupembedza mafano amene anawapanga ndi manja ao. Tsiku lina mfumuyo anaimika fano lalikuludi la golidi pa maso pa anthu onse. Analamulira anthu onse kuti apembedze fanolo. Iye anati, "Onse osagwadira ndi kulambira fanoli adzaponyedwa m'kati mwa ng'anjo yotentha yamoto." Koma analipo amuna atatu ompembedza Mulungu amene anakana kumvera lamulolo. Anali kukhulupilira kuti kuli Mulungu woona m'modzi yekha. Iwo sanafune kusamvera Lamulo Loyamba la Mulungu. Mfumu Nebukadinezara anayamba kukwiya kwambiri pakumva nkhaniyi yoti anthu ena sanali kufuna kumvera lamulo lace. Cifukwa cace iye anati, "Sonkhezani ng'anjo yotentha yamoto kasanu ndi kawiri loposa ndi kuwaponya amuna atatuwa m'kati mwace!" Citatha ici, motowo unali wotentha koposa kotero kuti atumiki amene anawaponya amunawo m'kati mwa ng'anjoyo anapsya ndithu. Koma amuna atatuwo amene anamvera Mulungu sanaphedwa ndi moto. Ngakhale tsitsi lao silinawauke konse. N'zoonadi Mulungu anatumiza mngelo Wace kuti awacinjirize ndi kuwapulumutsa iwo.

Amuna atatuwo, Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, anali anthu amene anamlemekeza, kumkonda, ndi kumkhulupilira Mulungu koposa zinthu zonse. Ici ndi cimene Mulungu afuna anthu onse kuti acite malinga ndi Lamulo Lace Loyamba. Iye akuti, "USAKHALE NAYO MILUNGU YINA KOMA INE NDEKHA." (Eksodo 20:3). Ici ndi cimene Mulungu M'modzi mwa Atatu anakamba. Ife ndiye Mulungu woona yekha. Iye amatiletsa kuti tisakhale nayo milungu yonama kapena ya mafano. Iye aumiliza kuti ulemelero wonse ndi cilemekezo conse ziperekedwe kwa Iye yekha (Yesaya 42:8).

Lamulo Loyamba limaswedwa ndi <u>iwo amene amapenbedza kapena kukhulupilira mulungu amene sali Mulungu M'Modzi mwa Atatu</u>. Anthu ambiri-mbiri amapanga mafano osema ndi mtengo, mwala, kapena citsulo. Ndithu, Mulungu analetsa ici momveka bwino (Eksodo 20:4). Masiku ano anthu a kumawa amagwadira maguwa a 'Buddha', Kapena ena amapemphera mulungu wonama dzina lace 'Allah' (Alaa). Ena amapemphera dzuwa, mwezi, kapena nyenyezi. Anthu ena amaikhulupilira mizimu ya makolo ao. Zinthu zonsezi ziri kupembedza mafamo. Koposa theka la anthu onse a m'dziko lapansi ali opembedza mafano. Angakhale ena amene amachedwa Akristu anapemphera milungu yonama poyera. Akatolika amapemphera Mariya. Mboni za yehova (Wacitawala) amapemphera Yehova, koma amamamukana Yesu Kristu kuti sali Mulungu woona. Yesu mwina akutsutsa kacitidwe aka momveka bwino (Yohane 5:23).

Koma Lamulo Loyamba limaswedwanso ndi <u>iwo amene amalamekeza ndi kukonda, ndi kutsimikizira mwacinsinsi cinthu ciri conse coposa Mulungu M'modzi mwa Atatu</u>. Anthu ambiri-mbiri amakonda ndalama kapena cuma koposa Mulungu. Yesu akutiuza kuti sitingathe kukhala akapolo a ambuye awiri (Mateyu 6:24). Mtumwi Yohane akuticenjeza pa ici mwa mphamvu (1 Yohane 2:15). Ngakhale anthu ena amadzikhulupilira mwa iwo okha kapena mu mphamvu yao yao koposa Mulungu. Mneneri Yeremiya awachula anthu oterewa—otembereredwa (Yeremiya 17:5).

Mulungu amafuna ife kuti <u>timlemekeze</u> Iye koposa zinthu zonse (Masalmo 33:8). Kumlemekeza Mulungu sikutanthauza kucita mantha ndi Iye, koma tiyenera kumcitira ulemu, osafuna kumcimwira Iye. Mulungu amafuna ife kuti <u>timkonde</u> Iye koposa zinthu zonse. Iye afuna kuti timpembedze ndi mitima yathu yonse (Miyambo 23:26). Martin Luther anati, "Cinthu cimene munthu amacikonda ndi mtima wace wonse ndi mulungu wace weni weni." Mulungu amafuna ife kuti <u>timkhulupilire</u> Iye Koposa zinthu zonse (Miyambo 3:5). Kumkhulupilira Mulungu kutanthauza kumtsimikizira Iye ndi Mau Ace ndi mitima yathu yonse.

MATHEDWE: Kuli Mulungu woona m'modzi yekha. Iye analenga zinthu zonse. Iye anapereka Mwana Wace kuti atifere ife. Iye anatipulumutsa kotero kuti tikhale anthu Ace ku nthawi yosatha. Ndiye cifukwa cace ife tiyenera kumukonda Iye koposa zinthu zonse nthawi zonse, monga adatilamulira mu Lamulo Loyamba. Tikapenyetsetsa mu mitima yathu, tingazindikire kuti timalephera kucita ici nthawi zambiri. Ndithu, cimo liri lonse limayamba mu mtima wa munthu. Tipemphe Mulungu kuti atikhululukire ife macimo athu ambiri wotsutsana ndi Lamulo Lace loyamba kaamba ka Yesu Kristu. Timufunse Iye kuti atipatse ife mphamvu yoposa yoti timkhulupilire Iye yekha.

Phunziro 7 - ZA LAMULO LOYAMBA

DZIWANI NKHANI (Danieli 3)

Lembani cizindikiro ici (✓) m'malo oyenera. Kapena amuna atatu a Mulungu kapena mfumu Nebukadinezara anazicita zinthu zotsatirazi:

	Amunua Atatu	Mfuma	
1.	( )	( )	anampembedza Mulungu woona.
2.	( )	( )	anampembedza mulungu wonama.
3.	( )	( )	anawalamulira ena kuti apemphere fano.
4.	( )	( )	anamkonda Mulungu koposa moyo.
5.	( )	( )	anamkhulupilira Mulungu kuti Iye adzapatsa thandizo.

PHUNZIRANI MAFUNSO

Maina a Mulungu woona ndiponso a milungu yonama kapena mafano akupezeka pansiwa. Lembani mzera wozimitsa maina a mafano:

YEHOVA	BAALA	MZIMU WOYERA
AMBUYE	ALLAH (ALAA)	DZUWA
MWANA WA NG'OMBE	ATATE WA MPHAMVU ZONSE	MWEZI
YESU KRISTU	CUMA	MULUNGU M'MODZI MWA ATATU

MUSANTHULE M'MALEMBO

Lembani mzera pansi pa ndime ya m'Baibulo imene ikutiuza kuti ndi kucimwa kukonda zinthu za m'dziko lapansi koposa Mulungu:

Miyambo 3:5 Eksodo 20:4 1 Yohane 2:15 Yohane 5:23

PHUNIZIRANI KATIKISIMU

LAMULO LOYAMBA

Usakhale nayo milungu yina koma Ine ndeka.

Kodi ici citanthauzanji?

Ife timlemekeze, kumkonda ndi kumukhulupilira Mulungu koposa zinthu zonse.